

Kuchokera mu Risale-i Nur

Pa Nkhanı  
Zokhudza Mwezi  
Wa Ramadhani  
Sherif

Wolembe  
Bediüzzaman Said Nursi



*Kuchokera mu Risale-i Nur*

*Pa Nkhani Zokhudza Mwezi Wa  
Ramadhani Sherif*

*Wolemba*

*Bediüzzaman Said Nursi*

## PA NKHANI ZOKHUDZA MWEZI WA RAMADHANĪ SHERĪF

Pamene timaliza gawo loyamba, takamba kale mwachidule “zizindikiro za chisilamu, mugawo lachiwiri ili mukambidwa za mwezi wolemekezeka wa Ramadhaan. Momwe muli chizindikiro chabwino ndi cha nzeru. Gawo ili liri ndi fundo zisanu ndi zinayi (9) zimene zifotokoza zinthu zosiyanasiyana zisanu ndi zinayi (9) za nzeru mu mwezi wa Ramadhaan.

بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِیْمِ  
شَهْرُ رَمَضَانَ الَّذِي اُنزِلَ فِيْهِ الْقُرْآنُ هُدًى لِّلنَّاسِ وَ  
بَيِّنَاتٍ مِّنَ الْهُدٰى وَالْفُرْقَانِ

## FUNDO YOYAMBA

Kusala m'mwezi wa Ramadhani sherifi ndi imodzi ya nsanamila zisanu za Chisilamu ndipo iyo ndi imodzi ya chizindikiro chachikulu chosunga Chisilamu.

Muli zolinga zambiri, ndiponso zinthu za nzeru, mu kusala m'mwezi wa Ramadhani sherif kumene kumayang'ana Ulamuliro wa *Jenab-I Haqq* (Allah, Mwini mphamvu zonse) ndi moyo wa munthu, ndi kuphunzitsa moyo wake wa uzimu, ndi kuonetsa kuthokoza kwake ku mphatso za *Jenab-i Haqq* Chimodzi cha zinthu za nzeru mu kusala chifukwa cha kulemekeza *Jenab-i Haqq* ndi ichi:

*Jenab-i Haqq* adalenga dziko m'maonekedwe a gome limene ndi lodzadza

ndi mphatso ndipo adaika pa gomeli mphatso ili yonse ngati kuonetsa:

مِنْ حَيْثُ لَا يَحْتَسِبُ

munjira imeneyi ali kufotokoza kukhazikika kwa Ufumu wake, chifundo ndi chisoni chake. Anthu amalephera kuzindikira chenicheni cha izi pamene ali pakati pa zinthu zina chifukwa chakusamva ndipo nthawi zina amaiwala. Komabe m'mwezi wa Ramazani, anthu okhulupirira, mwadzidzidzi, ngati gulu la anthu a nkhondo ophunzira bwino za ntchito yawo.

Pamene dzuwa liri kulowa, iwo amaonetsa machitidwe opembedza ngati kuti iwo aitanidwa ku chakudya cha Sultanii Ezeli, ndipo ali kuyembekezera chilamulo choti

“Igwani kuti mudzithandize nokha.”Iwo amavomela chifundo, chisoni chaponseponse ali kuzindikira ulemu ndi kupembedza kwa dongosolo. Kodi inu muganiza kuti anthu amene sachita nawo mapemphero ndi kupeza mphatso zolemekezeka ndi oyenera kutchulidwa kuti ndi anthu?

### **FUNDO YACHIWIRI**

Chimodzi cha chinthu cha nzeru chosala m'mwezi wodalitsikawa Ramadhani sheriff chokhudza kuthokoza Jenabii Haqq, chifukwa cha mphatso ndi ichi:

Monga zidanenedwa mu Mau Oyamba, kulipira chakudya chimene watchito amabweretsa kuchokera ku nyumba yophikira ya Mfumu. Koma kupereka kangachepe kwa munthu wobweretsa chakudya ndi kuganiza

kuti mphanso za mtengo wapatali kukhala zopanda pake ndiponso osazindikira Iye amene wapereka mphansozo, chikhoza kukhala uchitsiru wosasimbika.

Jenabii Haqq, adamwaza zinthu zambiri zabwino pa dziko lonse lapansi kuti munthu azigwiritsa ntchito ndipo pobwezera ubwino umenewu, Iye amafuna kuthokozedwa ngati malipiro a mphanso zimene adapereka.

Zimene zimayambitsa, ndiponso iwo amene amakhala nazo, ali ngati a ntchito onyamula chakudya. Ife timawalipira ndipo timakhala ndi ngongole ndi iwo, ngakhale kuti iwo siyenera, amalemekezedwa ndi kuthokozedwa. Pamene Nimetii İlahiy ndiye amene ayenera kulemekezedwa kwambiri kuposa anthu amene amatumidwa kudzapereka mphanso zimene ndi njira

zoperekera mphatso. Kumuthokoza Mun'im-ii Haqiqi ndi kuzindikira kuti mphatso zimachokera kwa Iye, ndi kuyamikira kuti ndi zabwino, ndi kuganizira za kufunikira kwake kwa munthu wolandira.

Kusala m'mwezi wa Ramadhan Sherif ndi makiyi oonetsa kuthokoza kwenikweni kuchokera pansu pa mtima chifukwa, mu nthawi zina za chaka, anthu ambiri amene sapeza mavuto sazindikira ubwino wa mphatso zambiri chifukwa iwo sagona ndi njala. Iwo amene mimba zawo zimakhala zokhuta, makamaka ngati ndi anthu olemera, sazindikira ubwino umene uli mu chingwa chouma. Koma pa nthawi yomasula kusala, kudya kumachitira umboni kuti chingwa chouma chija ndi mphatso ya mtengo wapatali ya uzimu m'maso mwa munthu wokhulupirira.



Mu nthawi ya Ramadhan-i Sherif , aliyense, kuchokera kwa Mfumu yaikulu mpaka munthu wamba, amaonetsa gawo lothokoza chifukwa chozindikira ubwino wa mphatsozo.

Popeza kudya ndi koletsedwa nthawi yamasana, iwo adzati: “Mphatso izi sizathu. Ife tilibe ufulu woti tizidye chifukwa ndi mphatso za munthu wina. Ife tidikira ulamuliro wa Nimetii İlahiye.” Iwo adzazindikira mphatso kuti ndi mphatso ndipo potero adzakhala ali kuthokoza. Motero, kusala mnjira imeneyi, munjira zambiri kuli ngati kiyi yothokoza chifukwa kuthokoza ndi udindo wokhazikika pa munthu.

## FUNDO YA CHITATU

China cha chinthu cha nzeru chosala m'mwezi wodalitsika wa Ramadhani sheriff chokhudza moyo wa munthu ndi ichi:

Anthu adalengedwa mosiyana pa nkhani zokhudza umoyo wawo. Chifukwa cha kusiyana uku, *Jenab-i Haqq*, amaitana anthu olemera kuti azithandiza anthu osowa ndi osauka kuti njala imene anthu amamva posala, anthu olemera akhoza kuzindikira ululu ndi mavuto amene anthu osowa ndi osauka amapeza. Pakadapanda kusala, pakadakhala anthu ambiri olemera amene sakanatha kuzindikira mmene njala imawawila, umphawi umapwetekera ndiponso mmene anthu osowa ndi osauka amafunira chithandizo.

Kuonetsa chisoni pa munthu mnzako ndi chinthu choonetsa kuthokoza kwenikweni. Ngati munthu, angakhale wotani, nthawi zonse padzakhala wina wake wosauka kuposa iye munjira zina. Motero iye amalamulidwa kuonetsa chisoni kwa munthu wotere. Ngati iye akadapanda kukakamizidwa kuti akhale ndi njala, iye sakanatha kumupatsa munthu wina, kudzera mukuonetsa chisoni, chithandizo chimene iye amayenera kupereka. Ndipo ngakhale kuti iye akanatha, chikadakhala choperewera chifukwa iye sanaone mmene njala imapwetekera.

### **FUNDO YA CHINAI**

China cha chinthu cha nzeru chosala m'mwezi wa Ramadhani sherif chokhudza kuphunzitsa munthu ndi ichi: chifukwa chakusamvera mzimu wa munthu umafuna

kukhala ndi ufulu ndi kuima pa okha ndipo umadziganizira wokha kuti ndi otero.

Malinga ndi chikhalidwe chake, munthu amaganiza kuti ali ndi ulamuliro pa yekha ndipo akhoza kuchita monga momwe afunira. Iye safuna kuvomereza kuti amasamalidwa ndi kuphunzitsidwa kudzera mu mphatso zosiyanasiyana. Makamaka ngati iye akhala ndi chuma ndi ulamuliro m'moyo uno, ndipo ngati kusamvera kumalimbikitsa iye, iye adzadya mphatso za Nimeti-i İlahiy monga momwe chinyama cholusa chimadyera.

Motero m'mwezi wa Ramadhani sherif, mzimu wa munthu aliyense, kuchokera kwa munthu wolemera kwambiri mpaka kwa munthu wosaukitsa, ukhoza kuzindikira kuti siwoyima pa okha ai, koma uli ndi mwini wake. Mau awa atanthauza kuti iye si mfulu ayi koma

kapolo. Iwo amazindikira kuti ngati sulandira lamulo, iwo siungathe kuchita chinthu ngakhale chaching'ono, iwo sungatambasule dzanja lake kutunga madzi. Maganizo ake oti ndi mfumu payekha amasokonezeka chifukwa amayamba kupembedza ndi kumathokoza, umene ndi udindo woonadi.

### **FUNDO YA CHISANU**

Chimodzi cha chinthu cha nzeru chosala m'mwezi wa Ramadhani sherifi, pochokera pa fundo yokonza makhalidwe a mtima wa munthu ndi kuti usiye machitidwe oipa ndi ichi: chifukwa chakusamvera mzimu wa munthu umadziyiwala okha. uwo sutha kuona kupanda mphamvu kwake, kusowa zinthu ndiponso kuchepa mphamvu mwa iwo okha, ndipo sufuna kuti uzidziwe.

Ndipo suganiza kuti ndi wofooka ndipo kudzera m'mavuto a nthawi ndi nthawi, kuti iwo ndi mnofu ndi mafupa chabe umene umaonda.

Mwachidule umalimbana ndi dziko ngati kuti udapangidwa ndi chitsulo ndipo umadziganizira kuti siungafe, ndikuti ndi wamuyaya. Umadziponya ku dziko mwa umbombo ndi kudya chakudya chochuluka. Iwo umakhala ndi chisangalalo ndiponso chikondi. Umakhutitsidwa ndi chinthu china chilichonse chimene chimachipatsa icho chisangalalo kapena chimene chimaupindulitsa. Motero umaiwala Mlengi wake amene amausamala mwa chisoni ndipo suganiza zotsatira za moyo wake ndiponso moyo wake m'dziko limene liri nkudza. Ndithudi, umasewera mu zinthu zoipa ndi zopanda makhalidwe.

Komabe kusala m'mwezi wa Ramadhani sherif kumapanga, ngakhale anthu osamva ndi a mwano, kudziwa kufooka kwawo, kusauka kwawo ndi kufuna chithandizo. Kudzera munjala, amaganiza za mimba zawo ndipo amadziwa chimene chili kufunika. Iwo amazindikira kusowa mphamvu kwa matupi ofoka, ndipo amaganiza za kufunika kwa chisoni ndi chikondi. Motero amasiya maganizo oipa onga a Firaun ndipo kudzera mu kufoka ndi kusowa mphamvu kwawo, amakhala ndi maganizo othawira kwa Rahmet.

Ndipo iwo amakonzeka kukagogoda pa khomo la chifundo ndi manja othokoza. Izi zimachitika ngati mwano ndi kusamvera sikunawaononge.

## FUNDO YA CHISANU NDI CHIMODZI

China cha zinthu za nzeru mu kusala m'mwezi wa

Ramadhani sherif, pa nkhani yokhudza chivumbulutso cha *Qur'an-I Hakim*, ndiponso kuti mwezi wa Ramadhani sherifndi nthawi yofunika kwambiri mu kuvumbulutsidwa kwake zil motere:

Popeza *Qur'an-i Hakim* lidavumbulutsidwa m'mwezi wa Ramadhani sherif, kusiya zilakolako za pansi za mzimu ndi zinthu zopanda pake, ndipo ndi kufanana ndi angelo posala chakudya ndi chakumwa ndi cholinga cholonjera uthenga wochokera kumwamba, mwanjira yabwino, ndi chimodzimodzi kukhala mdziko loyera.



Ndipo kuwerenga kapena kumvetsera *Qur'an-i Hakim* ngati kuti yangovumbulutsidwa, kumvera Uthenga wa Hitab-i İlahi ngati kuti uli kungovumbulutsidwa kumene, kumvetsera uthenga ngati kuti uli kuumva kuchokera kwa Resulullah, (*Aleyhis Salatu Wesellam*), ndithudi, kuchokera kwa Mngelo Jibril, (*Alleyhi ssalaam*), kapena kuchokera kwa Mutekkelimii Ezeli Mwini wake, ndi chimodzimidzi kukhala mdziko loyera. Kuchita mwanjira iyi ndi kuchita chimodzimidzi ngati munthu amene amamasulira mau ndipo kuthandiza anthu ena kuti amve uthengawu ndiponso munjira ina ndi kuonetsa nzeru zimene zili mu kavumbulutsidwe ka Qur'anii Hakim.

Ndithudi, zili ngati kuti dziko la Chisilamu limakhala Mzikiti mu nthawi ya Ramadhani sherifi. Pa kona iliyonse ya Mzikiti uwu, anthu

zikwi za zikwizikwi amene amadziwa Qur'anii Hakim pa mtima amapangitsa anthu amene amakhala pa dziko kumva mau ochokera kumwamba. Ndipo Ramadhani sherif iliyonse imaonetsa mau awa kukhala owala:

شَهْرُ رَمَضَانَ الَّذِي أُنزِلَ فِيهِ الْقُرْآنُ

Mau awa atsimikiza kuti Ramadhani sheriff ndi mwezi wa Qur'anii Hakim. Asilamu ambiri amamva anthu amene adaloweza Bukuli ali kulakatula mwaulemu pamene ena amaliwerenga pa okha.

Potsatira zilakolako za mtima pamene munthu ali mu Mzikiti, ndipo kusiya moyo wa chisangalalo podzera mu kudya ndi kumwa, ndithudi, ndi chinthu chokhumudwitsa ndipo chimamupanga munthu wotere kukhala

wonenedwa ndi anthu amene asonkhana mu Mzikiti. Munjira yomweyi anthu amene amatsutsa iwo amene amasala m'mwezi wa Ramadhani sherif, nawonso amalandira kunyozedwa kuchokera ku dziko lonse la Chisilamu.

### **FUNDO YA CHISANU NDI CHIWIRI**

China cha zinthu za nzeru mukusala m'mwezi wa Ramadhani sherif zokhudza kupindura kwa malonda a mtundu wa anthu, umene umadza mdziko lino ndi cholinga chokhala ndi chikonzero ndi kuchita malonda m'moyo umene uli nkudza zili motere:

Mphotho za ntchito za M'mwezi wa Ramadhani sherif ndi zochuluka zikwizikwi. Molingana ndi Hadth, lemba lirilonse la Qur'anii Hakim limakhala ndi mphotho khumi.

Liu lirilonse limawerengedwa ngati zabwino khumi ndipo lidzabereka zipatso khumi limodzi ku Ndalamadiso. M'mwezi wa Ramadhani sherif liu lirilonse silingabereke zipatso khumi limodzi koma chikwi chimodzi ndipo mavesi monga *Ayatul-Qur'siyyu* amabereka zikwizikwi pa liu lina lirilonse, ndipo pa tsiku la Chisanu lililonse la mwezi wa Ramadhani sherif, zimakhala zochuluka. Ndipo pa tsiku la *Layiatul-Qadri*, liu lirilonse limawerengedwa kuti liri ndi mphotho zikwi makumi atatu (30,000)

Ndithudi Qur'anii Hakim, limene liu lake lirilonse limabereka zipatso zosatha makumi atatu, liri ngati mtengo wodziwika wa Tuba umene M'mwezi wa Ramadhani sherif, umapezera anthu okhulupirira zikwi za zikwi za zipatso. Motero inu bwerani kuti mudzaone malonda a phindu ndi opatulika awa ndipo

mukatero muganize za iwo ndi kuzindikira kutaya zinthu kosatha kwa iwo amene salabadira kufunika kwa mau amenewa.

Mwachidule, Mwezi wa Ramadhani sherif ndi chionetsero cha phindu ndi msika wa malonda a moyo umene uli nkudza. Iwo ndi nthaka ya chonde chambiri ku mbeu za m'moyo umene uli nkudza. Pa nkhani zokula ndi kukhazikika kwa ntchito, kuli ngati mawawa a mvula ya mwezi wa *April* Icho chili ngati chikondwerero choonetsa kupembedza Kwa anthu pamaso pa Saltanati Rububiyetii ilahiy.

Popeza ndi choncho, mtundu wa anthu udalamulidwa kuti uzisala ndicholinga chakumvera, usamachite zinthu za unyama pofuna kukwaniritsa zilakolako zawo monga kudya ndi kumwa, kapena kuti usamachite

zinthu zonyasa. Pokhala pa mwamba pa unyama ndi kukana zinthu za pa dziko lapansi, munthu amakhala umoyo wa ungelu ndipo amachita malonda a moyo umene uli nkudza. Posala, iye amayandikira moyo umene uli nkudza ndi moyo wa uzimu umene umaoneka ngati thupi. Izi zimaoneka ngati kuti munthu wakhala galasi loonetsa Samediyetii İlahiy. Ndithudi, mwezi wa Ramadhani sherif uli ndi phindu lokhazikika ndi moyo wosatha mu dziko lino losakhalitsa ndiponso moyo wa kanthawi kochepea.

Ndithudi, mwezi umodzi wa Ramadhani sherif ukhoza kubereka zipatso zofanana ndi zipatso za moyo wa zaka makumi asanu ndi atatu. Choonadi ndi chakuti, malinga ndi nassi Qur'an Hakim limanena kuti usiku wa Laylatul Qadr ndi opambana kwambiri kuposa miyezi

yokwana chikwi chimodzi ndipo pali umboni wokwanira pa nkhaniyi.

Mwachitsanzo, Mfumu ikhoza kulamula kuti masiku ena akhale masiku a chikondwerero pa nthawi ya ufumu wake kapena kamodzi pa chaka. Masiku awa akhoza kukhala kukumbukira kwa kulowa ufumu wake kapena masiku ena amene awonetsa ulemerero wa Ufumu wake.

Pa masiku amenewa, iye amachitira anthu ake zinthu zabwino, zimene sizikhala mu chikonzero cha malamulo koma kudzera mu chuma chake cha pa dera, poonekera pa maso pa anthu ake osadzibisa. Ndipo iye amapereka zinthu mowolowa manja kwa anthu ake amene amakhala kumbuyo kwake kapena amene amadzipereka kwathunthu kwa iye.

Mwanjira yomweyiv Padishahii Zuljelal amene ndi mwini wa maiko zikwi khumi ndi zisanu ndi zitatu, amene ndi Sultanii Ezel ndi Ebed, adavumbulutsa m'mwezi wa Ramadhani sherif malamulo omveka amene ali mu limene limayang'ana maiko zikwi khumi kudza zisanu ndi atatu. Motero ndi koyenera kuti Ramadhani sherif iyenera kukhala chikondwerero cha padera, choonetsa cha mphamvu ya Qadiri Zuljelal ndi kusonkhana kwa uzimu popeza

Ramadhani sherif ndi chikondwerero, chimene Allah adalamula munthu kuti asale ndi cholinga chomuletsa mwa kanthawi, kuchita zinthu zapansi ndi za unyama.

Kusala kwabwino ndi kupanga nzeru za munthu ndi ziwalo zake monga maso, makutu, mtima ndi maganizo kuti zisale pamodzi ndi



mimba. Mau awa atanthauza kudziletsa kuchita zinthu zosaloledwa ndi zopanda pake, ndi kuzilimbikitsa zonse kuchita mapemphero kapena kupembedza.

Mwachitsanzo kuletsa lirime kuti lisaname, miseche ndi kutukwana, ndi kulipanga ilo kuti lisale. Ilo liyenera kutangwanika ndi zinthu zina monga kulakatula Qur'anii Hakim , kupemphera, kulemekeza Esmaili İlahiy (maina a Allah), kupempha madalitso a Allah kuti adze pa Mtumwi Muhammad (*Aleyhis Salatu Vesselam*), ndi *Istighfar* (kupempha chikhululukiro) cha machimo.

Mwachitsanzo kuletsa maso a munthu wa mwamuna kapena a munthu wa mkazi kuyang'ana munthu wa mkazi kapena wa mwamuna kunja kwa malamulo okhazikika, ndi kuletsa makutu kumva zinthu zoononga

koma mmalo mwake kugwiritsa ntchito maso kuphunzira, ndi makutu kumvera choonadi chimene chili mu Qur'ani Hakim ndi chimodzimidzi kupanga ziwalo zina kuti zisale. Kunena mwatchutchuchu mimba ndi fakitale yaikulu ndipo ngati iyo ilamula kupumula kugwira ntchito kudzera mu kusala, ndipo misonkhano ing'ono ing'ono idzatsatira malamulowa mosavuta.

## **FUNDO YA CHISANU NDI CHITATU**

China cha zinthu za nzeru mu kusala m'mwezi wa Ramadhani sherif, pa nkhani yokhudza moyo wa munthu ndi ichi: Ndi mankhwala ochiritsa, ndi chakudya cha padera cha uzimu chofunika kwambiri. Pamene munthu akudya, akumwa monga momwe afunira, zonse ndi zoononga ku moyo wa munthu potsatira malamulo a Umoyo. Ndipo

pamene iye adudukira china chilichonse chimene apeza osaganizira kaya ndi chololedwa kapena choletsedwa, icho chimaononga moyo wake. Ndiponso ndi chinthu chovuta kwa munthu wotere kuti amvere mtima ndi mzimu wake. Iye amatenga malamulo kukhala mmanja mwake ndipo potero iye sangalamulire chinthucho koma chinthucho chimamulamulira iye. Koma kudzera mu kusala m'mwezi wa Ramadhani sherif, amazolowera chakudya chimene amadya. Iye amayesetsa kudzisunga ndipo amaphunzira kumvera malamulo.

Ndiponso kudzakhala kuitana matenda a m'mimba pakudya chakudya chambiri pamene choyamba sichinasungunuke. Ndipo posiya, ngakhale ntchito zololedwa, monga iyo yalamulidwa, idzakhala ndi mwayi womvera malamulo a Chisilamu ndi chifukwa chake,

ndipo potero idzapewa zinthu zosaloledwa. Iyo sidzaononga moyo wake wa uzimu.

Ndiponso anthu ambiri amavutika ndi njala. Motero munthu amafunika kukhala ndi njala ndi kusunga mwambo, zimene ndi maphunziro ophunzitsa kupilira ndi kulimba pa mavuto. Kusala m'mwezi wa Ramadhani sheriff ndi kupilira ndi kulimba pa mavuto pa nthawi ya njala imene imapitilira maora khumi ndi asanu kapena maora makumi awiri ndi mphambu zinai, ngati chakudya cha m'bandakucha sichinadyedwe, ndiponso ndi kusunga mwambo ndi kuphunzira. Mau awa atanthauza kuti kusala ndi mankhwala a kusapilira ndiponso kufooka pa mavuto amene amakhala matenda a munthu.

Ndiponso fakitale ya m'mimba ili ndi ogwira ntchito ambiri. Ndipo ziwalo za anthu

zambiri zimalumikizidwa ku iyo. Ngati munthu sapuma kugwira ntchito nthawi yamasana, nthawi ya mwezi umodzi, zimapanga ogwira ntchito mufakitale, ndiponso ziwalo zimene zili mmenemo kuiwala maudindo awo. Chimawapangitsa iwo kukhala otangwanika ndi icho chokha ndipo izo zimakhala panso pa malamulo ake a nkhanza. Ndiponso chimasokoneza ziwalo zonse zimene zili m'thupi la munthu ndi utsi umene uli mu makina amene ali mufakitaleyo. Chimaitana chidwi chawo kwa iwo ndipo chiwapangitsa iwo, mwa kanthawi kochepe, kuiwala maudindo awo olemekezeka. Ichi ndicho chifukwa chake kuti mu zaka zikwizikwi, iwo amene ali kufupi ndi Allah, amakhala ndi chizolowezi chosunga mwambo ndi kumadya ndi kumwa zinthu zochepe kuti akhale angwiro.

Ndiponso kudzera mu kusala M'wezi wa Ramadhani sherif, ogwira ntchito mufakitale amazindikira kuti iwo sadalengedwe chifukwa cha fakitale yokha. Pamene ziwalo zina zonse, mmalo mosangalala mu zinthu zopanda pake, izo zimasangalala mu zisangalaso za angelo ndi zauzimu ndipo amayang'ana ku izo. Ichi ndicho chifukwa chake kuti m'mwezi wa Ramadhani sherif, anthu okhulupirira amapeza mpumulo, zipatso zambiri ndi chisangalalo cha uzimu zimene zimasiyana malinga ndi ulamuliro wake. Zida zawo monga mtima, mzimu, luntha, zimachita zinthu zopambana mu mwezi wodalitsikawu kudzera mu kusala. Iwo amaseka ndi chimwemwe ngakhale kuti mimba imalira.

## **FUNDO YA CHISANU NDI CHINAI**

China cha zinthu za nzeru mu kusala m'mwezi wa Ramadhani sheriff pa nkhani yozunguza maganizo a munthu odzikweza ndi kumudziwitsa kupembedza pomulangiza kufooka kwake ndi ichi:

Mzimu wa munthu sufuna kuzindikira amene amausamala. Iwo umafuna ufumu wakewake monga Firaun. Ngakhale kuti iwo umapeza mavuto ambiri, makhalidwe awa amakhalabe mu iwo. Komabe iwo umaonongedwa kudzera mu njala. Motero, kusala mmwezi wa Ramadhani sheriff kumakhoma nkhonya zolimba mu mtima wolingana ndi Firaun ndi kuwazunguza. Iwo umaonetsa kulephera, kufooka ndi kufuna chithandizo. Icho chimaupangitsa iwo kuzindikira kuti ndi a kapolo.

Pakati pa mafotokozedwe a Hadith ya mtumwi wa Allah pali kafotokozedwe aka:

*“Janab-I Haqq, adati kwa Mzimu wa munthu:*

*“Kodi Ine ndani, nanga iwe ndani?”*

Mzimu uja udayankha

*“Ine ndine, ndipo Iwe ndiwe Iwe.”*

Motero Allah adaulanga iwo ndipo adauponya mu ng’ango ya Moto.

Ndipo adaufunsanso, ndipo iye anayankha

*“Ene ene, ente ente.”*

Motero adaulanganso koma iwo sudasiye kudzikweza.



Pomaliza adaulanga ndi njala. Kutanthauza kuti moto udamusiya iye ndi njala.

Ndipo Allah adafunsanso

“Men ene vema ente?”

Ndipo Mzimu uja udayankha

أَنْتَ رَبِّي الرَّحِيمُ وَأَنَا عَبْدُكَ الْعَاجِزُ:

“Iwe ndiwe Msamali wanga wa chifundo ndipo

Ine ndine kapolo wako wopanda mphamvu.”

اللَّهُمَّ صَلِّ وَسَلِّمْ عَلَى سَيِّدِنَا مُحَمَّدٍ صَلَاةً تَكُونُ لَكَ  
 رِضَاءً وَ لِحَقِّهِ آدَاءً بَعْدَ ثَوَابِ قِرَاءَةِ حُرُوفِ الْقُرْآنِ  
 فِي شَهْرِ رَمَضَانَ وَ عَلَى آلِهِ وَ صَحْبِهِ وَ سَلِّمْ  
 سُبْحَانَ رَبِّكَ رَبِّ الْعِزَّةِ عَمَّا يَصِفُونَ وَسَلَامٌ عَلَى  
 الْمُرْسَلِينَ وَ الْحَمْدُ لِلَّهِ رَبِّ الْعَالَمِينَ آمِينَ

**Hasiye:** gawo lachiwiri linalembedwa mwachangu pamene ine mwini ndi bukhu limene ndimalembamo ndinali mkudwala, popeza linalembedwa mofulumira choncho silinaikidwe mu ndondomeko wake ndiponso mwina munalakwika. Tikudikira kuchokera kwa abale athu kuti alione ndikulankhulapo mopanda kudzudzulidwa. Ndipo angathe kukhozamo m'mene angaganizile.

**Contact Us:**

**salihbayrakdar@gmail.com**

**+265998570464**